

“Kulenga Chikhalidwe Cha Uzimu”

“Lolani kufatsa kwanu kudziwike ndi anthu onse, Ambuye ali pafupi. Musadere nkhawa pa chirichonse: koma mu chinthu chirichonse mwa pemphero ndi pembedzero pamodzi ndi chiyamiko lolani zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu, umene umadutsa kumvetsa konse, udzasunga mitima yanu ndi malingaliro kupyolera mwa Khristu Yesu. Chotsalira, abale, zinthu zirizonse zoonza, zinthu zirizonse zolemekezeka, zinthu zirizonse zolungama, zinthu zirizonse zoyera, zinthu zirizonse zokondeka, zinthu zirizonse zomveka mokoma: ngati pangakhale ukoma uliwonse, ndipo ngati pangakhale chitamando china, ganizirani pa zinthu izi.” (Afilipi 4:5-8).

Ndipo kodi inu mumadziwa, inu ndi mlengi wang’ono, inu eni? Inu mukudziwa zimenezo? Ndithudi. Inu mwawaonapo anthu amene inu mumangokonda kukhala nawo pafupi. Inu osadziwa chifukwa chake. Basi mtundu umenewo wamunthu wokonda. Inu munayamba mwaona zimenezo? Wachifundo basi, pamenepo, inu mumakonda kukhala pafupi nawo. Iwo amalenga chikhalidwe chimenecho, ndi moyo umene iwo amakhala, mmene iwo amayankhulira, machezedwe awo.

Ndiye inu, mwaonapo iwo amene, nthawi iliyonse, inu mumathawa iwo. Nthawi zonse, iwo amafuna kuti ayankhule china chake choipa, ndi kuyankhula zokhudza wina wake. Iwo amanyozapo wina wake pamenepo. Iye ali mkati muno tsopano iye ayankhula zokhudza munthu uyu. Zonse zoti iwo achite ndi kunena nthabwala zauve. kapena china chake monga choncho. Iwe umangodana nazo kukhala pafupi ndi iwo. Mukuona? Iwo amalenga. Woneka, wokongola anthu abwino okongola, koma iwo amalenga chikhalidwe chimenecho.

Ndipo zinthu zimene inu mumaganizira, zinthu zimene inu mumachita, machita-chita, zinthu zimene mumayankhula, zimalenga chikhalidwe. [1]

Dziko likufa kwa chikondi: Mpingo ukufa kwa chikondi. Yesu anati, “Inu muli mchere wa dziko lapansi.” (*Mateyu 5:13*). Koma ngati mchere wataya kukolera kwake, iwo ndiye siumakhalanso wabwino, koma kuti ukapondedwe ndi mapazi a anthu. Ngati mpingo wataya vumbulutso la uzimu lake la chikondi cha Mulungu, iwo umakhala chotonza, ndi mphesi, ndi chopunthwitsa ku dziko. (1 *Yohane 4:7-8; 16*).

Tsopano, pali chinthu chimodzi chokha mpingo ukuyenera kuchita. Ngati iwe ukufuna wina wake kuti abwere kwa Khristu, khala wokolera mchere kwambiri. Mchere umapangitsa ludzu; inu mukhale okolera mchere kwambiri ndipo dziko lidzakhala ndi ludzu. Ndiko kulondola.

Pakuti mwa munthu, iye ali mu mphamvu imodzi mlengi wang'ono ngati iye ali mwana wa Mulungu, chifukwa Mzimu wa Mulungu uli mwa iye, umene umalamulira iye, umene umagwiritsa iye ntchito.

Koma ine nkanakonda kukulolezani inu pa zinthu zina monga izi, chikondi chamzimu chanji... Tsopano mvetserani, Paulo anati, “Pamene pali malirime, inu adzatha. Pamene pali uneneri, iwo udzalephera.” (1Akorinto 13:8-12). Pamene pali zizindikiro zonse izi... wotsutsa Khristu akhoza kutulutsa chizindikiro chirichonse chimene chiri mu Baibulo, koma iye sangakhoze kukonda. Kulibe kanthu kwa iye kuti akonde.

O, inu mutha kukhala ndi mtundu wina wa chikondi cha bodza. Pali mitundu iwiri ya chikondi. Pali chikondi chimene chimatchedwa chikondi cha munthu kapena mu mawu achigiriki, icho chikana tchedwa, “Fileo.” Ndipo mu chikondi cha umulungu chiri Agapao. Chikondi cha Agapao chiri chikondi cha umulungu. Ndipo pamene chikondi cha umulungu chiri mu mtima wanu, muli kusiyana mu moyo wanu, ndipo munthu aliyense amadziwa izo. Ndiko kulondola. Inu mumakhala moyo monga Mkhristu, umachita monga Mkhristu, umayenda monga Mkhristu; ndipo kachitidwe kanu konse kali koikidwa munthawi ku Baibulo la Mulungu.

Tsopano, ngati iwe umamukonda Mulungu kwenikweni... Ndipo iwe ukudziwa pali anthu ena ake amene ali anthu abwino kweni kweni, kokha iwe sungakwanitse kuima kuti ukhale pafupi ndi iwo. Ndiko kulondola. Chifukwa chiyani izo ziri? Iwo analenga chikhalidwe chimenecho. Ndipo pali mtundu wina wa anthu umene iwe umangokonda kukhala nawo pafupi. Iwo amalenga chikhalidwe chimenecho chomwe iwo amakhalamo. [2]

Ndipo pozungulira iye wadzadzidwa ndi Mzimu.

Ndi chiyani icho? Ndiyo mphamvu yakulenga imeneyo yomwe ili pa anthu yimene amalenga chikhalidwe mozungulira kumene iwo ali. Ngati iwo ali wodzala ndi chikondi, osati kudzipanga kukhulupilira, koma chikondi chenicheni, iwe ungate kumverera icho. Iwe umadziwa kuti iwo ali a Khristu. Iwo amagwedeza dzanja lako, nati, “Ndine mnzako, Joni.” Iwe ungate kumverera izo. [3]

Mwaona, inu muli mlengi wa chikhalidwe pozungulira inu. Ndipo inu mumazipanga zimenezo nokha mwa maganizo anu anu ndi Mzimu umene uli mkati mwa inu. [4]

Tsopano, chiri chinthu chautimu. Tsopano, pamene kukhalapo kwa Ambuye kubwera pansi, iko kumalenga chikhalidwe kwa chikhulupiro.

Tsopano, inu mukuyenera kulenga chikhalidwe, ndipo chikhulupiro chanu chidzachita izo. Iwo onse anali mu chipinda chapamwamba ndi cholinga chimodzi, pamene mwadzidzidzi apo kunadza kuchokera kumwamba monga mphokoso la mkokomo wa mphepo ya mphamvu; chikhalidwe chinali choyenera (*Machitidwe 2:1-4*). Izo zimatengera chikhalidwe kuti uchite chirichonse.

Inu mukudziwa, kachitidwe ka chizolowezi kuti zibalitse anapiye ndi kuwayika iwo pansi pa nkuku. Koma tengerani dzira mu chikhalidwe choyenera, ilo lidzaswa mulimose. Mvetserani, m'bale, ngati munthu amakonda Mulungu, ndipo mtundu woyenera wa chikhalidwe iye angakhoze kulowamo, izo zidzatulutsa mwana wobadwa kumene motsimikiza basi monga ine ndili pano (*Yohane 3:3-5*). Ndi chikhalidwe chimawerengeredwa. Lorani anthu ochepa odzadza m'manja awa akhala panowa, afike mu chikhalidwe changwiro, penyani chomwe chingachitike. Sipangakhale wofooka pakati pathu. Wolumala adzayenda; akhungu adzapenya; agonthi adzamva; wosayankhula adzayankhula wopanda pemphero kapena chirichonse. Ndi chikhalidwe.

Ndimomomwe mazana makumi awiri ndi asanu anachiritsidwa pa pemphero limodzi mu Africa. Pamene iwo anawona Ambuye akuchita china chake, izo zinalenga chikhalidwe, ndipo iwo analowa mu icho. Ndilo dziwe pamene madzi akuthamanga moyenera. (*Yohane 5:1-4*). [2]

Ndipo kupatula njere ya tirigu igwera mu nthaka, iyo imakhala yokha (*Yohane 12:24*). Ndiyeno pamene Mawu abweretsedwe mu mtima wa chikhulupiro, zimenezo zimapangitsa kuti lonjezo llirilonse mu Baibulo likhale moyo kachiwiri. Mukuona? Iwo akuyenera kukhala moyo. Iwo ndi Mawu wophuka, ndipo iwo akuyenera kukhala moyo ngati iwo alandiridwa mu malo woyenera. Pansi pa zikhalidwe zoyenera, mbewu iliyonse idzakhala moyo kachiwiri, ngati iyo iyikidwa pansi pa chikhalidwe choyenera.

Ndipo abale, mundilore ine ndinene izi ndi kulemekeza ndi ulemu kwa inu monga abale anga, podziwa kuti mwina usanafike usiku ife tonse tidzaima pa mpando wa chiweruziro wa Khristu m'mwamba..... (*Aroma 14:10-13*;

2 Akorinto 5:10-11; 1 Akorinto 3:11-15). Ndipo yang'anani, mundilore ine ndinene ichi: chiri chikhalidwe nthawi zonse chimene chimabalapo zotsatira. [5]

Inu mukhoza kuika mbewu kunja uko mu nthaka. Ziribe kanthu mochuluka motani mbewu imeneyo ili ndi chomuletsa, ndipo yayikidwa iyo pamenepo, iyo ikuyenera kukhala nacho, chikhalidwe kuti chipange iye kukhala moyo. Mukuona? Dzuwa limenelo likuyenera kufika pa mphamvu ina yake, kuyibweretsa iyo kuchikhalidwe chinachake. Dzira layenera kukhala nacho chikhalidwe, kapena ilo siligogomola. Ziribe kanthu momwe liliri lachonde ilo, ilo layenera kukhala nacho chikhalidwe.

Uwu ndi mtundu wa chikhalidwe ine ndinabadwiramo. Ziribe kanthu komwe ine ndipita, ndi kucheza dziko lozizira, ndi m'minda ya mtumiki ndi zina zotero, ine ndingathe ngakhale kuima ndi kutseka maso anga ndi kumaganiza za chikhalidwe ichi. [6]

Tsopano, Baibulo linati Mawu a Mulungu ndi Mbewu imene wodzala anadzala (*Mateyu 13:1-9; 18-23*). Inu alimi pano, kodi inu mukudziwa kuti pamene mudzala mbewu, ngati mudzala tirigu, bwanji, uyo adzabereka tirigu, ngati uyo ayikidwa mu chisamaliro choyenera. Inu mudzala therere, ilo lidzabala therere mu chisamaliro chake choyenera.

Chabwino, ndicho chomwe Mawu a Mulungu ali. Ngati inu mutenga Lonjezo lirilonse la Mulungu ndi kuliya ilo mu Chikhalidwe choyenera, ilo lidzatulutsa ndendende chomwe ilo liri mu Moyo wake.

Ngati ife tingapeze mtundu woyenera wa chikhalidwe chamwamba, chinachake chidzachitika. Mukuona? Chikhalidwe. [7]

Ife tikusowa kuti tiwonetsa Mawu awa kachiwiri. Osawayika iwo osati pamtanda, pa msomali, koma pachikhalidwe chamoyo cha Mzimu Woyera. Izo zimabweretsapo zotsatira. Mawu a Mulungu, pansi pa chikhalidwe choyenera, adzawonetsera ndendende chomwe iwo anati iwo adzachita. Iwo akuyenera kuti akhale mu chikhalidwe choyenera. Ngakhale Inu simungakhoze kuwaika iwo mu seminary, kapena sukulu ya Baibulo ina yake yimene simakhulupilira mu zizindikiro ndi zodabwitsa. Iwo sadzabowoleza konse ndi kubweretsa moyo pamenepo. Chikhalidwe ndi cholakwika. Koma inu mukuyenera kuti muike izo mu chikhalidwe choyenera. Ndi mtundu wani wa chikhalidwe? Chikhalidwe chodzipereka. Khalani pamenepo mpaka icho chitapita ku kukula ndi kutenga moyo. [8]

Ndipo Yesu anati cha mu *Marko 11:22*, “Ngati inu munena kwa Phiri ili, sunthidwa, ndipo osakaika mu mtima wanu, koma kukhulupilira chomwe inu mwanena, icho chifika pochitika.” Mukuona? Kukhulupilira

kuti chomwe iwe wanena, ndipo Mkhristu ali wolembedwa kwambiri kuti pozungulira iye ndi chikhalidwe.

Kodi inu munayamba mwakumanapo ndi anthu amene inu basi munakonda kukhala nawo? Inu mwakhalapo nazo zimenezo, ndipo chifukwa chiyani, iwo amalenga chikhalidwe chimenecho ndi moyo wawo, momwe zinakhalira moyo, ndi zinthu iwo amaganizira, ndi chikondi iwo ali nacho kwa inu.

Inu mumalenga chikhalidwe, ndipo ndicho chikhalidwe inu mukuyenera kuti mukhalemo kuti mupempherere kwa odwala. Mukuona? Ndicho chinthu chofanana. Ndicho chikondi chimene chimatulutsa mizimu yoyipa. [9]

O, Mulungu, ndilo pemphero langa, dzutsani mpingo kachiwiri kukachitidwe kachikale, misonkhano yapemphero ija usiku wonse. Dzutsirani anthu ku chikhalidwe chauzimu. O, zimatengera zimenezo kuti zibweretse ana mu ufumu. Izo zimatengera khalidwe.

Ndipo ndizo zomwe zimatengera mu mpingo lero, osati kachikhulupiliro kokhutala mochuluka kwambiri ndi za Umulungu. Koma Mzimu wa Mulungu wamoyo ukutsanuliridwa pansi pa anthu Ake kuti ukabweretsa chikhalidwe cha uzimu, wopanda mmodzi akuti, “Ine ndikukhulupilira izo ndi ichi.” Ndipo mmodzi wina, “Ine ndikukhulupilira izo ndi icho.” Izo ndi zolimba kwa Mzimu Woyera kuti ugwire ntchito.

Ndipo ndizo zomwe tikusowa lero, abale. Ife tiri kumbuyo kwambiri. Mpingo unayenera kukhala ma mailosi miliyoni pamwamba pa msewu.

Pamene ife titenga monga chomwe chinachitika cha uko mu Africa tsiku lina pamene m'bale wathu wofunika Gilly Grahama, pamene Wachihindu anatulukira pamenepo ndi kupanga chitsutso monga choncho kutsutsana ndi Mawu a Mulungu wamoyo, izo zinasonyeza ife tikusowa chikhalidwe china mmalo mwa za Umulungu. Ife tikusowa mphamvu ya Mzimu Woyera pakati pathu, ndi amuna amene ali wolorera kukaima pa chomwe Mulungu akunena kukakhala choonadi. Ndicho chikhalidwe chimene ife tikusowa.

Mwina mwake mu tsiku lalikulu ili la kuchita bwino, kuti ife takhala tiri wokondweretsedwa mukuchita bwino mpaka ife tachoka kuchinthu chenichenicho. Mwina mwake ife tasochera pa mtundu wina wake wa kukwiya wopanda lye. Ife sitikuyenera kuchita zimenezo. Ndilo khalidwe. Ndi pamalo amene ife tikufuna Khristu. [10]

Ndiyo njira izo ziri pamene munthu akhala wobadwa kachiwiri. Pali china chake chimachitika mkati mwake, chimene iye ali wodwala ndi otopetsedwa nalo dziko. Ndipo pali Mzimu wa umulungu pafupi naye.

Koma moyo wanga wakhala ukuchita nazo zinthu zauzimu, monga inu mukumvetsa mu msonkhano. Iwe umayenda kupita kwa anthu nthawi zina, amene amayesa kuti atengere chinachake. O, m'bale, Branham, ine ndikutsimikiza ndili nacho chikhulupiliro mwa inu. Ndipo iwe umadziwa iye akunama. Mukuona? Pali Mzimu pamene umene umayankhula mokweza kwambiri kuposa milomo yake yoyankhula. Ndicho chikhalidwe.

Ndipo ngati iwo uphunzira kukonda ndi kukhala wachifundo kwa aliyense, ndi kukhala wodekha, kukhala nacho chipiliro, izo ngakhale zidzapanga moyo wapanyumba yako kusiyana. Izo zidzapanga woyanjana nawo ako kusiyana. Mulungu adzakulemekeza iwe. Tsopano, ine ndayeserapo izo.

Tsopano, chinthu chokha, iwe ukuyenera kusintha kachitidwe. Ngati zimenezo zingathe kuchitika mnyumba, izo zingathe kuchitika mu mpingo; izo zingathe kuchitika mu fuko; izo zingakhoze kuchitika mudziko lonse. Ndilo khalidwe limene limawerengedwa.

Kotero ndi khalidwe. Ndipo inu mumapanga khalidwe limenelo ndi chomwe inu muli mkati mwa inu. [3]

Ndipo, O, kodi inu simukanakonda kukakhala pafupi ndi Yesu pang'ono chabe. Zodabwitsa! Kuwona chomwe khalidwe limenelo lye analenga likanakhala liri, ine ndikulungalira ilo linali basi mutu wa ukuru wopambana wa chikondi, ndi ulemu, ndi kuopa kwa Umulungu. [11]

Tsopano, Yesu anatipatsa ife chitsanzo cha chomwe ife tikuyenera kuti tikhale tikuyang'anirapo, pamene lye ananyezimiritsa moyo Wake kwa ife kupyolera mmawu, chomwe ife tiyenera kuwona. Pamene ife tayang'anira mu kalilore wa Mulungu, ife tiyenera kudzionika tokha tikuzindikiritsidwa ndi lye. Ndicho chitsanzo cha mngwiro.

Tsopano, koma ife tikupeza kuti, pamene ife tikupita kudutsa mmoyo, kuti khalidwe lathu limawomba chifanizo cha chimene ife tiri. Mmudzi aliyense amadziwa zimenezo. Inu, pamene mukukhala moyo, chotero liri khalidwe lina, limakuwumbani inu kuchomwe inu muli. Tsopano, inu mwawonapo anthu amene inu mumakonda kukhala chifupi nawo, komabe iwo angathe kusakhala kwenikweni mu gulu lanu loyanjana nalo. Ndipo kachiwiri, iwo angathe kukhala a mtundu wosiyana, achikuda, kapena abrawuni, kapena achikasu. Koma pali china chake basi chokhudza khalidwe limenelo, chimene inu mumangokonda kukhala mukukhalapo kwawo. Chifukwa munthu aliyense ali dynamo wang'ono wa iwo eni, ndipo inu mumatulutsa chikhalidwe.

Ndiyeno, inu mumawona anthu amene anali anthu wolemekezeka, komabe inu munali nthawi zonse wokondwa kuchoka kwa iwo. Izo ziri basi iwo amalenga chikhalidwe choterechi mozungulira pamene inu muli. Palibe kanthu kotsutsa iwo, iwo ali anthu abwino, koma inu basi simukonda chikhalidwe chimenecho, iwo alimo. Ndipo khalidwe lawo limalenga chirichonse iwo ali, zimapanga iwo chomwe iwo ali. [12]

O, ngati iwe uli nacho chizindikiro, iwe umalenga Mzimu mozungulira iwe, mphamvu, kuti pamene iwe uyenda, anthu amadziwa kuti ndiwe Mkhristu. Iwo amakonda kwa iwe kuti unene china chake kwa iwo. Iwo amakhulupilira mawu ako. Chomwe iwe unena, iwo amagwiritsa ku icho. Mukuona? Ndi zimenezotu. Pakani chizindikiro, ndiye yendani ndi Icho.

Ndiye pakani chizindikiro mu pemphero, ndi kuganizira, ndi kukhulupilira. Pakani icho ndi chikondi chotero, ndi zina zotero, mpaka inu mutadziwa izo ziri zoti zichitike. Ndizo zonse. Pakani Icho mu chidaliro, khulupilira Icho chiri choti chithandize. Pamene muyankhula kwa mwana ameneyo, pamene uyankhula kwa mamuna wako, uyankhula kwa mkazi wako, uyankhula kwa wokondedwa uyu, khulupilira kuti Icho chiri choti chithandize. Ingoima pamenepo, ndi kunena, “Ambuye, ine ndikuwatenga iwo. Iwo ali anga, ine ndikuwatengera iwo kwa Inu, Ambuye.”

Gwiritsani ntchito Icho, ndipo lengani chikhalidwe chimenecho pozungulira inu, kuti iwo angogwira kumene mu Icho. Tengani apanyumba yanu. Inu mukuyenera kuchita izo tsopano. Iyi ndi nthawi yakumadzulo. Tsopano, inu mwakhala mukumvetsera kwa nthawi yaitali, tsopanoiyi ndi nthawi yakumadzulo. Ndi nthawi yogwiritsa ntchito tsopano. Mkwiyu ukantha limodzi la masiku awa, izo zikhoza kukhala mochedwa pamenepo. Pakani chizindikiro, ndi chidaliro. [13]

Tsopano, Baibulo ndi bukhu losiyana kwa bukhu lopatulika lina lirilonse. Palibe bukhu longa Baibulo, chifukwa Baibulo ndi Mulungu mumawonekedwe a Mawu. Mawu ndi lingaliro litalongosoledwa. Kuganiza kwa Mulungu kunawalongosola iwo, Mawu Ake kupyolera mwa aneneri; ndipo iwo analemba Baibulo, lomwe liri m'mawonekedwe a Mawu. Ndipo Yesu analitcha Ilo, “Mbewu.” Ndipo mbewu iliyonse idzalora mwa mtundu wake ngati iyo ili mu chikhalidwe choyenera, pamalo oyenera. Bukhu ili launeneri, ilo limaneneratu, zodzachitika Mtsogolo. Tsopano, Bukhuli liri ndi Vumbulutso lonse la Yesu Khristu. Inu simumawonjezera kwa Ilo kapena kuchotsako kwa Ilo, ndipo

vumbulutso lililonse liyenera kumabwera ndi Ilo. Mwaona, izo ziyenera kumakhala Mawu. [14]

Chifaniziro:

- [1] "Moyo Wanu Uli Woyenera ndi Uthenga?" (63-0630E), ndime 151.
- [2] "Chikondi Cha Umulungu" (57-0305), ndime E14-18.
- [3] "Chikondi" (57-0519E), ndime. E15-16, E17-18, E23.
- [4] "Musachite Mantha Ndi Ine" (62-0629), ndime. E44.
- [5] "Zotsatira za ulendo waku India" (57-0126B), ndime. E26-27.
- [6] "Chotsamvetsetseka" (64-0531), ndime. 11-12.
- [7] "Tiwonetseni lfe Atate" (61-0521), ndime E61
- [8] "Mfumukazi yaku Seba" (61-0219), ndime. E38
- [9] ".Izo Sizinali Choncho Kuchokera Pachiyambi" (60-1127M), ndime. E7-8
- [10] "Ndine Musachite Mantha" (60-0329), ndime E19-20.
- [11] "Kumdutsa Yesu" (63-0117), ndime 24.
- [12] "Chizindikiritso" (63-0123), ndime. 40-42.
- [13] "Chizindikiro" (63-0901M), ndime. 373-375
- [14] "Zochitika zamakono zimamveka bwino ndi uneneri" (65-1206), ndime. 46.

Mwala womangira wauzimu No. 53: Kuchokera ku Mawu Owululiridwa a ora ino, Osindikizidwa ndi: Gerd Rodewald, Friedenstr. 69, D-75328 Schomberg, Germany

www.biblebelievers.de, Fax: (+49) 72 35 33 06

Kukubwera m'modzi ndi Uthenga umene wulunjika ku Baibulo, ndi mofulumira ntchito ya kuzungulira Dziko lonse. Mbewu idzalowa manyuzi pepala, Mu zipangizo zowerengera, mpaka mbewu yosankhidwiratu ndi Mulungu idzamva izo.

[M'bale Branham, "Mu Buku la Chikhalidwe- Dongosolo- Chiphunzitso cha Mpingo," Tsamba 724]